## KUBWERANSO KWA YESU

"*Pakuti Ambuye adzatsika kumwamba mwini yekha ndi mfuu, ndi mawu a mgelo wamkulu, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka; pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nawo pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mlengalenga,, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse.*" **1 Atesalonika 4v16-17**

## KODI IZI ZIZACHITIKA LITI?

Pali zinthu zambiri zomwe zikuchitika pa dziko lapansi ndipo anthu ambiri akukhulupilira kuti Yesu abwera posachedwa. Pa Mateyu 24, Yesu akutipatsa chithunzithunzi cha zinthu zomwe zikuyenera kuchitika pa dziko lonse lapansi Iye asanabwere. Pa **Mateyu 24v1-5**, pamene Yesu anafunsidwa za zindikiro zakubweranso kwake komanso kutha kwa nthawi, choyambilira chomwe ananena ndi choti: "*Yang'anirani, asasokeretse inu munthu pakuti ambiri adzafika mdzina langa, nadzanena ine ndine Khristu, nadzasokeretsa anthu ambiri*." Chenjezoli ndilofunika ndipo Yesu akulibwereza pa **Mateyu 24v11,24**, komanso akulankhula za akhristu onama, aneneri onyenga, komanso mazunzo akulu. Akunena pa **Mateyu 24v24** kuti "*Onani, ndakuuziranitu pasadafike*." Pa mavesi amenewa, Yesu akutichenjeza mwamphamvu kuti tikonzekere kukumana ndi mazunzo akulu. Choncho, tiyeni tione Buku lonse la Mateyu 24.

**Mateyu 24v6-7** akuti kuzakhala nkhondo, njala, zivomerezi. Zinthu izi ziri ponseponse.
**Mateyu 24v8** akuti ichi ndi chiyambi cha zowawa za mzimayi obereka, kutanthauza kuti zowawa zazikuru zitsatirapo. Ngati Tsunami yomwe yachitika ku Japan ikufanizidwa ndi zowawa zoyamba; tiyembekezere zowawa zazikuru zotani?
**Mateyu 24v9-13** akukamba za chisautso cha akhristu: imfa, udani, kutaya chikhristu komanso chinyengo cha aneneri onama. Mu nyengo iyi uchimo udzachuruka ndipo "*chikondi cha ambiri chidzazilala*" **(Mateyu 24v12)** ndipo ndichifukwa **Mateyu 24v13** akutichenjeza kuti tikhalebe mwa Khristu, akuti: "*koma iye wakulimbika chilimbikire kufukura ku chimaliziro, yemweyo adzapulumuka.*"

**Mateyu 24v15-22** akufotokozanso za chisautso ndikuuza a Yuda onse okhala ku Yudea kuti athawe pamene otsutsa Khristu aonekera mukachisi yaku Yerusalemu chifukwa kuonekera kwake kudzakhala chiyambi cha zowawa zazikulu zomwe sizinaonekenso pa dziko lapansi (awa akutchedwa mazunzo akulu). **Mateyu 24v22** akufotokoza kuti nyengo iyi idzakhala yoyipa ndipo masiku awa adzafupikitsidwa chifukwa cha akhristu.
**Mateyu 24v23-24** akubwereza kuchenjeza zokhudza aneneri onyenga komanso a khristu onama amene adzachita zozizwa zazikulu ndi cholinga choti akanyenge osankhikawo. Pa **Mateyu 24v24** Yesu akuchenjeza: "***ONANI NDAKUUZIRANITU PASANAFIKE***"

Pa **Mateyu 24v26,29**, atatichenjeza za akhristu onama, Yesu akuti kubweranso kwake, diso liri lonse lidzamuona monga mphenzi iwonekera kummawa mpaka kumadzulo. Akutiuza kuti tisakhulupilire pamene anthu anena Khristu ali pano kapena ali uko, koma tiyang'anire chizindikiro chapadera cha kubweranso kwake. Chizindikiro ichi chaperekedwa pa **Mateyu 24v29** pamene akuti: "*dzuwa lidzadetsedwa, ndi mwezi suzaonetsa kuwala kwake, ndi nyenyezi zidzagwa kuchokera kumwamba, ndi mphamvu zakumwamba zidzagwedezeka*" chitachitika chizindikiro ichi, pamenepo, Ambuye adzabwera.

Choncho, Mateyu 24 watiuza izi:-

- kudzakhala nkhondo, njala, zivomerezi kenaka
- otsutsa Khristu adzazibvumbulutsa yekha mu kachisi kenaka
- Akhristu ndi a Yuda adzazunzidwa ndipo
- Akhristu onama komanso aneneri onyenga adzanamiza ambiri kenaka
- padzakhala chizindikiro cha dzuwa, mwezi komanso nyenyezi.

**Mateyu 24v30-31** akutiuza kuti chizindikiro ichi chitaoneka m'mitambo, Yesu adzafika m'mitambo ndipo maiko adzalira chifukwa adzadziwa kuti atsala pang'ono kuonongedwa. **Mateyu 24v31** akuti nthawi iyi, Yesu adzatuma angelo ake ndi liwu la lipenga kusonkhanitsa (mkwatulo) onse osankhika kukakhala ndi Iye pamene mkwiyo wa Mulungu udzathilidwa pa dziko lapansi, kumalizira ndi nkhondo ya Amagedoni.

Ndizomveka bwino kuti mpingo ukuyenera kuona otsutsa Khristu ndikudutsa mu masautso akulu Khristu asanabwere kudzatenga okhulupilira ndikuononga ochimwa.

## 2 ATESALONIKA 2V1-3

**2 Atesalonika 2v1-3** akutionetsanso kuti mkwatulo uzachitika pokhapokha okana Khristu ataonekera. Vesili likufotokoza kuti: "*Ndipo tikupemphani abale, chifukwa chakudza kwake kwa Ambuye wathu Yesu Khristu, ndikusonkhana pamodzi kwathu kwa iye;* [mkwatulo] *kuti musamagwedezeka mtima msanga ndikutaya maganizo anu, kapena kuopsedwa mwa mzimu kapena mwa mawu; kapena mwa kalata monga wolembedwa ndi ife, monga ngati tsiku la Ambuye lafika; munthu asakunyengeni konseko; kuti silifika koma chiyambe chifike chipatukocho, nabvumbulutsike munthu wosayeruzika,* [okana khristu] *mwana wa chionongeko."* Mavesi amenewa akufotokoza momveka bwino kuti akhristu sadzasonkhanitsidwa pamodzi pokhapokha okana Khristu ataonekera, ndipo izi ndizomwe Mateyu 24 akufotokoza.

## 1 ATESALONIKA 4V13 – 5V11

Akhristu ambiri amakhulupilira kuti 1 Atesalonika 4v13-5v11 amakamba za msonkhano wina wa Ambuye. Amakhulupilira kuti mavesi amenewa amanena kuti Yesu adzakwatula mpingo okana Khristu asanaonekere. Koma tebulo liri pansili likusiyanitsa 1 Atesalonika 4-5 ndi Mateyu 24-25 ndipo likufotokozera momveka mfundo zomwe zikukamba za chinthu chimodzi.

**Chart 1**
**Kusiyanitsa 1 Atesalonika 4-5 ndi Mateyu 24-25**

| | Zochitika | 1 Atesal. | Mateyu |
|---|---|---|---|
| 1 | Kubweranso kwa Khristu | 4v16 | 24v30 |
| 2 | Kuchokera ku mwamba | 4v16 | 24v30 |
| 3 | Ndi mfuu | 4v16 | 24v30 [Ndi mphamvu] |
| 4 | Ndi angelo | 4v16 | 24v31 |
| 5 | Ndilipenga la Mulungu | 4v16 | 24v31 |
| 6 | Mkwatulo | 4v17 | 24v31, 40-41 |
| 7 | Okhulupirira akumana ndi Ambuye | 4v17 | 25v1,6 |
| 8 | Mu m'mitambo | 4v17 | 24v30 |
| 9 | Nthawi sikudziwika | 5v1-2 | 24v36 |
| 10 | Adzabwera ngati mbala | 5v2,4 | 24v43 |
| 11 | Pakati pa usiku | 5v2 | 24v43 |
| 12 | Osakhulupirira sakudziwa zachiweruziro | 5v3 | 24v37-39 |
| 13 | Chiweruziro chidza ngati zowawa za mzimayi woyembekezera | 5v3 | 24v8 [cf. RSV] |
| 14 | Okhulupirira asanyengedwe | 5v6 | 24v4-5,25 |
| 15 | Okhulupirira apenyerere | 5v6 | 24v42,25 |
| 16 | Chenjezo kwa oledzera | 5v7 | 24v49 |

Kusiyanitsa kwa 1 Atesalonika 4-5 ndi Mateyu 24-25 kukufotokozera chinthu chimodzi. Kubweranso kwa Yesu kudzachitika kamodzi ndipo izi zidzachitika okana Khristu ataonekera ndikuzunza Israeli komanso mpingo. Pamene Yesu abweranso adzakwatula osankhidwa ake kenako mkwiyo wa Mulungu udzatsanulidwa pa dziko lapansi.

**CHIBVUMBULUTSO 6-8**

Chitsimikizo china chofotokoza zochitika Yesu asanabwere, monga Mateyu 24 akufotokozera, chikupezeka mu tebulo liri pansili. Tebuloli likufanizira Mateyu 24 ndi Chibvumbulutsa 6-8.

Chart 2
Kusiyanitsa Mateyu 24 ndi Chibvumbulutso 6-8

| | Mateyu 24 | | Chibvumbulutso cha Kristu | |
|---|---|---|---|---|
| 1 | 24v4 | Chenjezo | 22v19 | Chenjezo |
| 2 | 24v5 | Akhristu onyenga | 6v1-2 | Chizindikiro choyamba |
| 3 | 24v6 | Nkhondo | 6v3-4 | Chizindikiro chachiwiri |
| 4 | 24v7 | Njala | 6v5-6 | Chizindikiro chachitatu |
| 5 | 24v9,21 | Mazunzo akulu | 6v7-8 | Chizindikiro chachinayi |
| 6 | 24v9,22 | Imfa | 6v9-11 | Chizindikiro cha chisanu |
| 7 | 24v10,24 | Kutaya chikhulupiriro | | |
| 8 | 24v29 | Chizindikiro cha masiku otsiriza. Dzuwa, mwezi ndi nyenyezi | 6v12-17 | Chizindikiro cha chisanu ndi chimodzi |
| 9 | 24v30,27 | Chizindikiro cha kubweranso kwa Khristu | | |
| 10 | 24v30 | Kubwera kwa Khristu | | |
| 11 | 24v13,31 | Mkwatulo | 7v9-14 | Khamu lalikulu |
| 12 | 24v14,30, 37-39 | Mkwiyo wa Mulungu | 8v1-7 | Chizindikiro cha chisanu ndi chiwiri |

Yesu mwini wake watipatsa Mateyu 24 ndi Chibvumbulutso 6-8, komanso chitsimikizo choti Mateyu 24 ikukamba za zinthu zomwe zikuyenera kuchitika Yesu asanabwere.

Mavesi ena monga Luka 17v22-35 komanso 2 Atesalonika 1v6-11 akutionetsa kuti tsiku lina Yesu adzabwera kudzakwatula anthu ake komanso kupereka chilango kwa ochimwa omwe adzatsale pa dziko lapansi.

**OKANA KHRISTU**

Okana Khristu ndi munthu amene adzadzadzidwe ndi mphamvu ya satana, kapena kunena kuti satana kuonekera kuthupi, kudzera mwa okana Khristu. Satana adzayesa kuononga Israeli komanso mpingo ndicholinga choyimitsa malingaliro a Mulungu pa munthu, chifukwa akudziwa kuti malingaliro a Mulungu akakwaniritsidwa, iye adzaponyedwa mu nyanja ya moto kwa muyaya. (Chibvumbulutso 20v10)

Tikuuzidwa kuti satana adzapatsa okana Khristu mphamvu zake. Pa **Chibvumbulutso 12v7-17** akuti kudzakhala nkhondo kumwamba ndipo Mikaeli adzakankhira chinjoka chokalamba (satana) pa dziko lapansi. Pamenepo, satana adzakhala ndi mkwiyo ndipo adzazunza Israeli (v13) komanso akhristu (v17). Adzachita izi kudzera mwa okana Khristu. Pa **Chibvumbulutso 13v1-2** okana Khristu akutchedwa *"chilombo chochokera*

*kunyanja"* ndipo tikuuzidwa kuti "*chinjoka chokalamba* [satana] *chinapatsa chilombo mphamvu zake, ufumu wake, ndi ulamuliro wake waukulu.*" **Chibvumbulutso 13v7** akuti "*Ndipo anachipatsa icho kuchita nkhondo ndi oyera mtima, ndikuwalaka, ndipo anachipatsa ulamuliro wa pa pfuko liri lonse, ndi anthu, ndi manenedwe, ndi mitundu."* Choncho okana Khristu adzakhala ndi mphamvu zazikulu za satana ndi ulamuliro kuzunza ndi kunamiza ambiri.

**2 Atesalonika 2v3-4** akutiuzanso zokhudza okana Khristu. Mavesi amenewa akuti: "*munthu asakunyengeni konseko; kuti silifika koma chiyambe chifike chipatukocho, nabvumbulutsike munthu wosayeruzika,* [okana khristu] *mwana wa chionongeko, amene atsutsana nazo, nadzikuza pazonse zotchedwa Mulungu, kapena zopembedzeka; kotero kuti iye wakhala pansi ku kachisi wa Mulungu, nadzionetsera yekha kuti ali Mulungu"* komanso **2 Atesalonika 2v9-10** akutiuza kuti: "*ndiye amene kudza kwake* [okana khristu] *kuli monga mwa machitidwe a satana, mu mphamvu yonse, ndi zizindikiro ndi zozizwa zonama; ndi m'chinyengo chonse cha chosalungama kwa iwo akuonongeka popeza chikondi cha choonadi sanachilandire kuti akapulumutsidwe iwo."*

Choncho tikhoza kuona kuti satana adzapatsa mphamvu kwa okana Khristu kuti azunze anthu a Mulungu komanso kuchita zozizwitsa zonama ndi cholinga chonamiza anthu kuti akhulupilire kuti iye ndi Mulungu. Chifukwa cha mphamvu zochuluka za okana Khristuyo; Yesu akuchenjeza akhristu mobwereza kuti tisanamizidwe koma tiime chilili kufikira chimaliziro, komanso kudikira kubweranso kwake komwe kudzakhale ngati mphenzi, ndipo kudzachitika chizindikiro cha dzuwa, mwezi ndi nyenyezi chitaoneka.

## NDICHIFUKWA CHIYANI AKHRISTU AKUYENERA KUZUNZIDWA?

Anthu ambiri amati Mulungu sangalole anthu ake akomane ndi zowawa ndi okana Khristu. Pambali pa masautso amene akunenedwa mu baibulo, **Afilipi 1v29** akuti: "*kwapatsidwa kwa inu kwa ufulu chifukwa cha Khristu, si kukhulupilira kwa Iye kokha, komatunso kumva zowawa chifukwa cha Iye"* komanso **Aroma 8v17** akuti: "*ndipo ngati ana, pomweponso olowa nyumba, inde olowa nyumba ake a Mulungu, ndi olowa anzake a Khristu ; ngatitu ife timva zowawa pamodzi naye, kuti tikalandirenso ulemerero pamodzi ndi Iye."* Yesu akunena pa **Yohane 15v20** kuti : "*kumbukirani mawu amene ndinanena kwa inu, Kapolo sali wamkulu ndi mbuye wake. Ngati anandilonda londa ine, adzakulonda-londani inunso; ngati anasunga mau anga, adzasunga anunso."* Choncho sikoyenera kunena kuti Mulungu sangalole anthu ake kuti amve zowawa. Nanga Mulungu amalola izi bwanji pamene ali ndi mphamvu yoziletsa?

**Ahebri 2v10** akuti Yesu analungamitsidwa kudzera mu zowawa komanso **1 Petro 1v6-7** akutiuza kuti kudzera mu kumva zowawa, chikhulupiliro chathu chimayesedwa ndikukometsedwa monga golidi akonzedwa mu moto. Choncho mazunzo amatilungamitsa monga analungamitsa Yesu. **Aroma 5v3-5** akuti tikondwere m'masautso athu pakuti: "*Ndipo sichotero chokha, komanso tikondwera m'zisautso; podziwa ife kuti chisautsochichita chipiliro, ndi chipiliro chichita chizolowezi; ndi chizolowezi chichita chiyembekezo; ndipo chiyembekezo sichichititsa manyazi chifukwa chikondi cha Mulungu chinatsanulidwa m'mitima mwathu mwa Mzimu Woyera amene wapatsidwa kwa ife."* 2 Akorinto Paulo akukamba za kuzunzidwa mobwereza, ndipo pa **2 Akorinto 7v4** akuti: "*ndilimbika mtima kwambiri pakunena nanu, kudzitamandira kwanga chifukwa cha inu nkwakukuru; ndidzadzidwa nacho chitonthonzo, ndisefukira nacho chimwemwe m'chisautso chathu chonse."* komanso **Mateyu 5v11-12** Yesu akuti: "*Odala muli inu m'mene adzanyazitsa inu, nadzazunza inu, nadzakunenerani monama zoipa ziri zonse chifukwa cha Ine. Sekerani, sangalalani; chifukwa mphotho yanu ndiyaikuru m'Mwamba: pakuti potero anazunza aneneri anakhalawo musanabadwe inu."*

Choncho Mulungu amagwiritsa ntchito kuzunzidwa kuyesa chikhulupiliro chathu, kutilungamitsa komanso kutitsogolera ku mphotho yaikuru kumwamba. Lonjezo la Mulungu ndilakuti Iye adzakhala ndi ife nthawi zonse, kutithandiza munthawi ya zowawa. **Aroma 8v35-39** Paulo akuti palibe chimene chingatilekanitse ndi chikondi cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu Yesu komanso **2 Timoteo 1v11-12** Paulo akulankhula za kuzunzidwa kwake ndi kudalira Yesu kumusamalira - "*umene ndaikikapo mlaliki, ndi mtumwi ndi mphunzitsi wake. Chifukwa cha ichicho, ndinamva zowawa izi, komatu sindichita manyazi pakuti ndimdziwa Iye amene ndamkhulupilira , ndipo ndikopeka mtima kuti ali wamphamvu ya kudikira chosungitsa changacho kufikira tsiku lijalo."* Muzaka zonse, akhristu ambiri akhala akuzunzidwa , ena kuphedwa chifukwa cha chikhulupiliro chao ndipo Yesu amakhala pafupi nawo nthawi zonse. Choncho ifenso tikhoza kutsimikizika kuti Iye adzakhala nafe mu masautso athu.

Ngati tingapilire mazunzo akulu komanso chisautso chimenechi, tikuyenera kufunafuna kupezeka kwa Ambuye chifukwa akutichenjeza kuti "*ndipo pomwepo ambiri adzakhumudwa, nadzaperekana wina ndi mzake.. koma iye wolimbika chilimbikire kufikira ku chimaliziro, yemweyo adzapulumika."* **(Mateyu 24v10,13)** Choncho tiyeni timvere machenjezo a Ambuye komanso kuphunzira kuyenda chifupi ndi Iye.

Pomaliza, **Yuda 1v24** akutitonthoza motere *"ndipo kwa Iye amene akhoza kukudikirani mungakhumudwe ndi kukuimikani pamaso pa ulemelero wake wopanda chirema mkukondwera."*

Tonse tinene "*Yehova ndiye mphamvu yanga ndi chikopa changa; mtima wanga wakhulupilira Iye ndipo ananndithandiza*." (**Masalimo 28v7**)

Contact: Pastor Sam D Phiri
Cell Phone: 0884 157558 or 0993 564671
Email: samdinala@yahoo.com

Written by: Mick Alexander
Email: leeandmick@gmail.com
www.ChristianIssues.biz